



MUTU 8:

CHIPANGANO  
CHATSOPANO,  
KUBADWAKWA  
KHRISTU, NDI  
MAYESERO AKE

---

6 B.C.

INU MULLUNGU WA  
ABRAHAMU, ISAKE, NDI  
YAKOBO, NDAKHALA  
NDIKUDIKIRA MPULUMUTSI,  
KOMA SINDIKHALITSA.

ZOONADI SUKHALITSA,  
KOMATU UDZAMUONA  
WOLONJEZEDWAYO  
USANAMWALIRE.

SIMEONI ANAFUFUZA  
M'MALEMBO OYERA NDIPO  
ANAPEZAMO MAULOSI  
AMBIRI OKHUDZA KHRISTU.




SIMEONI, UMABWERA KUNO  
TSIKU LILILONSE. NDIKANAKONDA  
ANSEMBE ONSE AKANAKHALA  
ODZIPEREKA NGATI IWE.



KODI UNENERI UWU WA YESAYA  
WOKHUDZA KHRISTU UKUTANTHAUZANJI?  
YESAYA AKUTI NAMWALI ADZAKHALA NDI  
PAKATI NDIPO ADZABALA MWANA  
WAMWAMUNA. AMENEYU AYENERA KUKHALA  
MBEU YA MKAZI, MONGA MOMWE  
MULLINGU ADANENERA KWA HAVA.



INDE, YESAYA ADATINSO  
MWANAYO ADZATCHEDWA  
MULLINGU WAMPHAMVU. KOMA  
SICHAPAFUPI KUMVETSA  
TANTHAUZO LA UNENERI.



POTSATA MIKA 5:2,  
MWANA NGWACHIKHALIRE  
MONGA MULLINGU AMENE,  
PENANSOTU NDI PA SALIMO  
45:6 PAMENE MULLINGU  
AKUTCHULA MWANA KUTI  
MULLINGU.


NDI OCHEPA  
AMENE  
ADZAVOMEREZANA  
NAWE, NCHIFUKWA  
CHAKE SUYENERA  
KUYANKHULA ZIMENEZI  
PA GULU; AKHOZA  
KUKUPHA POKUGENDA  
NDI MIYALA.

MUDZAONA. NDISANAFE,  
MESIYA ADZABWERA M'KACHISI  
MOMWE MUNO, NDIPO  
NDIDZAMUONA.



NKUTHEKA KUTI  
AKUNENA ZOONA.


IWE NDIWE YANI?  
UKUDZIWA CHIYANI ZA  
ZINTHU IZI?



INE NDIMANGOMVERA  
ZOKAMBIRANA ZANUZO.  
INENSO NDAKHALA  
NDIKUWERENGA MALEMBO  
OYERA, NDIPO ZAKA 500  
ZAPITAZO DANIELE ADANENA  
ZINTHU ZOPATSA CHIDWI  
ZOKHUDZA NTHAWI YA  
KUBWERA KWA MESIYA.

KODI IWE LINGADZIWE  
ZIMENE ALEMBI A  
MALAMULO SADZIWA?





ATATE ANGA NDI MLEMBI WA MALAMULO NDIPO  
ANDIONETSA ZIMENE ANENERI ADALOSA. MULLINGU  
ADAUZA DANIELE KUTI KUCHOKERA PA NTHAWI IMENE  
LAMULO LINAPEREKEDWA KUTI YERUSALEMU  
AMANGIDWENSO KUFIKIRA PAMENE MESIYA  
ADZAPHEDWA PADZAPITA ZAKA 483.

TSOPANO PAPITA ZAKA 449  
CHIPEREKEDWERE CHA LAMULOLO.  
NDIYE KUTI KWANGOTSALA ZAKA  
34 ZOKHA, TSONO NKUTHEKA  
KUTI MESIYA ANABWERA KALE  
PAKATI PATHU.

GENESIS 3:15; SALIMO  
45:6; YESAYA 7:14, 9:6;  
DANIELE 9:25-26; MIKA  
5:2; LUKA 2:25-26




LUKUZIDZIWA  
BWANJI  
ZIMENEZI?

IYAI, ASANABWERE.  
MZIMU WOYERA  
ANANDIULLULIRA KUTI  
NDISANAFE  
NDIDZAONA MESIYA  
WAKHANDA M'KACHISI  
MOMWE MUNO.

MUDZAONA.


PAMENE SIMEONI  
ANKAKALAMBIRAKALAM  
BIRA NAMADIKIRABE  
M'KACHISI,  
KUYEMBEKEZA  
KHRISTU  
WOLONJEZEDWAYO,  
WANSEMBE WINA  
WOTCHEDWA ZEKARIYA  
ADAPITA KU KACHISI  
KUKAPEMPHERA. IYE  
NDI MKAZI WAKE ANALI  
OKALAMBA NDIPO  
KUFIKIRA NTHAWI IYI  
ANALI  
ASANABEREKEPO  
MWANA.



MWADZIDZIDZI MNGELO  
ANAONEKERA KU  
DZANJA LAMANJA LA  
GUWA LA NSEMBE!


USAOPE. PEMPHERO  
LAKO LAMVEKA NDIPO  
MKAZI WAKO  
ELIZABETI ADZABALA  
MWANA WAMWAMLUNA,  
NDIPO UZAMUTCHE  
KUTI YOHANE.

AMBIRI ADZASANGALALA  
MWANAYO AKADZABADWA,  
CHIFUKWA NDIYE AMENE ADZAUZA  
ANTHU KUTI AKONZEKERE KUBWERA  
KWA MESIYA. SADZAMWA VINYO  
KAPENA CHAKUMWA CHILICHONSE  
CHAUKALI NDIPO ADZALANDIRA  
MZIMU NDI MPHAMVU ZA ELIYA.



NDINGADZIWE BWANJI KUTI  
ZIMENE MUKUNENAZO NDI ZOONA?  
INE NDI MKAZI WANGA NDIFE  
OKALAMBA KWAMBIRI, NKOVUTA  
KUTI TIBALE ANA, NDIPO MKAZI  
WANGA WAKHALA WOLIMA MOYO  
WAKE WONSE.

INE NDINE **GABIRIELE**,  
AMENE NDIMAKHALA KUFUPI  
NDI MULLINGU, NDIPO IYE  
WANDITUMA KUDZAKUUZA ZIMENEZI.  
KODI UKUFUNA CHIZINDIKIRO?  
UDZAKHALA WOSAYANKHULA KUFIKIRA  
ZINTHU IZI ZITAKWANIRITSIDWA.



NDIDZAKHALA  
WOKONDWA POKAMBA  
ZIMENEZI. M'NYUMBA  
UMU MULI ZII.  
MUSAMAYANKHE  
ANGELO  
AKAMAKUYANKHULANI,  
MWAMVA!

ZAKARIYA, MPOVUTA KUZIKHULLUPIRIRA  
ZIMENEZI. MONGA SARA, MAI WA FLUKO  
LATHU, MULLINGU WAMVA MAPEMPHERO  
ATHU, NDIPO POSACHEDWAPA NDIKHALA  
MAI WA MNENERI WAMKULU.

KWA ZAKA 4,000, ANENERI ADAKHALA AKULOSA ZA MESIYA WODZABWERAYO. ZAKA 700 M'MBUYOMO MNENERI YESAYA ADATI; "ONANI NAMWALI ADZATENGA PATHUPI, ADZABALA MWANA WAMWAMLUNA, NDIPO ADZAMUTCHA DZINA LAKE IMANUELE, MULLINGU ALI NAFE"



MARIYA ADAPALIDWA LIBWENZI NDI YOSEFE. MARIYAYO ANALI ASANAGONEPO NDI MWAMUNA WINA ALIYENSE. ANKAMVERA MALAMULO ONSE A MOSE.




MWADZIDZIDZI, MNGELO  
ADAONEKERA MARIYA!

MARIYA, MULLINGU  
WAKUKOMERA MTIMA  
KWAMBIRI. UZATENGA  
PATHUPI NDIPO UZABALA  
MWANA WA MULLINGU.

ZIMENEZI ZINGATHEKE  
BWANJI POPEZA INE  
SINDINAGONEPO NDI  
MWAMUNA ALIYENSE?





MZIMU WOYERA WA MULLINGU  
ADZAKUPHIMBA. MWANA WOYERA  
AMENE UDZAMUYEMBEKEZERA ADZAKHALA  
MWANA WA MULLINGU. MSUWENI WAKO  
ELIZABETI, AMENE ANTHU ANKATI  
NGOSABALA, NDI WOYEMBEKEZERA  
TSOPANO. UNO NDI MWEZI WAKE  
WACHISANU NCHIMODZI.



INE NDINE KAPOLO  
WAMKAZI WA AMBUYE.  
ZIKHALE KWA INE MONGA  
AMBUYE AKUFUNIRA.

NDIDZAKHALA MAI WA  
MWANA WA MULLINGU. KODI  
YOSEFE ADZANDIKHULLUPIRIRA? KODI  
ADZAZIMVETSA ZIMENEZI? KODI ANTHU  
ADZAGANIZA CHIYANI AKADZAMVA ZOTI  
NDINE WOYEMBEKEZERA? BASI;  
NDIKAKHALA NDI ELIZABETI.



***ELIZABETI!***

***MARIYA,  
MWANA  
WANGA!***

NDIWE WODALA MWA  
AKAZI ONSE, NDIPO  
NCHODALITSIKANSO  
CHIPATSO CHA M'MIMBA  
MWAKO. INE NDINE YANI  
KUTI MAI WA MULLINGU  
ABWERE KUDZANDICHEZERA?  
POPEZA PAMENE NDINAMVA  
MAI AKO, MWANA AMENE  
ALI M'MIMBA MWANGA  
ANATAKATAKA NDI  
CHIMWEMWE.

MOYO WANGA  
UKULEMEKEZA  
MULLINGU, NDIPO MZIMU  
WANGA WAKONDWERA  
NDI MULLINGU  
MPULUMUTSI WANGA.  
ZIKADZACHITIKA IZI,  
MIBADWO YONSE  
IDZANDITCHA WODALA,  
POPEZA AMBUYEYO  
WACHITA ZINTHU  
ZAMPHAMVU.





WAKWEZA ENAFE PAMENE  
NDIFE OCHOKERA KU MABANJA  
OSAIKA. MONGA ADANENERA  
KWA KHOLO LATHU ABRAHAMU,  
IYE WATIKUMBUKIRA MWA  
CHIFUNDO CHAKE.

MARIYA ANACHEZA NDI ELIZABETI  
PAFUPIFUPI MIYEZI ITATU.



NTHAWI YOTI ELIZABETI  
ABALE MWANA INAFIKA.

ZEKARIYA AKUTI  
AMENEYO ADZAKHALA  
MWANA WAMWAMUNA; AKUTI  
MNGELO NDIYE ADAMUZA  
CHONCHO.

CHABWINO,  
AKAKHALA MWANA  
WAMWAMUNA NDIYESA  
ADZATCHEDWA ZEKARIYA  
POTSATA DZINA LA  
ATATE AKE.

NDI LIYO  
AKUBWERA  
APOYO.  
TIMUFUNSE.



AKUTI MNGELO NDIYE  
ADAMUCHITITSA KUTI  
ASAMAYANKHULE CHIFUKWA  
SADAKHULUPIRIRE.

MWANAYO  
MUDZAMUTCHA DZINA  
LOTI CHIYANI?

AKUFUNA POTI  
ALEMBEPO.

AKUTI DZINA LAKE  
ADZATCHEDWA YOHANE,  
MONGA MOMWE MNGELO  
ADAMULAMULIRA.

KOMA  
M'BANJAMU  
MULIBE AMENE  
AMADZIWIKA NDI  
DZINA LOTI  
YOHANE







NDI MNYAMATADI,  
MNYAMATA WA CHEYA  
CHAMBIRI.



**DZINA LAKE NDI  
YOHANE, POTSATA MAU A  
AMBLIYE. ADZAONETSA MESIYA  
KWA AISRAELE, ANTHU A  
MTUNDU WATHU.**

**AKLIYANKHULA!  
PATAPITA MIYEZI  
YONSEYI, TSOPANO  
AKLIYANKHULA!**

**KODI TINENE  
KUTI AMENEYU  
NDI ELIYA  
POTSATA MAU  
A ANENERI?**

KENAKA, YOSEFE  
ANAZINDIKIRA KUTI MARIYA  
ANALI NDI MIMBA, NDIPO  
ANADZIWA KUTI MIMBAYO  
SINALI YAKE.



AMAI,  
SINDIKUKHULUPIRIRA  
BE. ANALIBENSO  
ZIBWENZI ZINA  
KUPATULA INE.  
SACHOKA PAKHOMO  
PA MAKOLO AKE.  
SINDINACHITE  
ZIMENEZO. KOMA  
NKHANI NDI  
IMENEYO. ALI NDI  
PATHUPI.



IWE YOSEFE,  
LICHITA CHIYANI?

SINDIMKWATIRA,  
KOMANSO SINDIKUFUNA KUTI  
ANTHU AZIDZIWE ZIMENEZI.  
AKHOZA KUMUGENDA NDI MIYALA  
POMUGANIZIRA KUTI WACHITA  
CHIGOLOLO. MWINA  
TINGOFULUMIRA KUTHETSA  
LBWENZIWI.



AKUTI MWANA  
AKUYEMBEKEZERAY  
O NGWAYANI?

AKUTI BAMBO WA  
MWANAYO NDI MULLINGU,  
MWANAYO ADAIKIDWA  
M'MIMBA MWAKE NDI MZIMU  
WOYERA OSATI MONGA  
MOMWE ZIMACHITIKIRA KUTI  
ANTHU ATENGE  
PATHUPI.



**AAA! KOMA MUTU  
WAKE UKUGWIRA?**


**AKUTI  
MWANAYO  
ADZAKHALA  
MPULUMUTSI WA  
DZIKO LONSE,  
MWANA WA  
MULLINGU.**

**NDI MWANOTU KUTI  
MAI ANENE ZOTEREZI.  
NDIYENERA KUMULEKA  
MSANGAMSANGA.**

A muscular man with dark curly hair, wearing a yellow vest with circular details and a white loincloth, stands in a dark, stone-walled environment. He is gesturing with his right hand towards the right. The background is dark with some architectural lines.

**USIKU UMENEWO, YOSEFE  
AKUGONA, MNGELO ANAMUFIKIRA.**

**YOSEFE, IWE MWANA  
WA DAVIDE, USAOPE KUTENGA  
MARIYA KUTI AKHALE MKAZI WAKO,  
POPEZA MWANA AKUYEMBEKEZERAYO  
ADAIKIDWA M'MIMBA MWAKE NDI  
MZIMU WOYERA. ADZABALA MWANA  
WAMWAMLUNA NDIPO UDZAMUTCHA  
DZINA LAKE YESU, POPEZA  
ADZAPULUMUTSA ANTHU  
AKE KU MACHIMO AO.**



**KUMENEKU NDI  
KUPHEREZERA MAU A  
MNENERI YESAYA: "NAMWALI  
ADZATENGA PATHUPI, ADZABALA  
MWANA WAMWAMLUNA NDIPO  
ADZAMUTCHA DZINA LAKE  
IMANUELE, KUTANTHAUZA KUTI,  
'MULLUNGU ALI NAFE.'"**






MARIYA  
UNDIKHULLUKIRA  
MOTANI CHIFUKWA  
CHOKUKAIKIRA?

NDIKUDZIWA, NZODABWITSA.  
MWA AKAZI ONSE A MU  
ISARELE NDI MWA AKAZI ONSE  
PA ZAKA ZIKWIZIKWI ZAPITAZO,  
MULLINGU NKUSANKHA INE  
KUTI NDIBALE MESIYA WA  
DZIKO LONSE LAPANSI!



KODI MWANAYO  
ADZAKHALA WOTANI? POTI  
ADZAKHALA MULLINGU, NGAKHALE  
AZIDZAONEKA NGATI IFE, KODI  
AKADZABADWA AZIDZAYANKHULA?  
KODI ADZAKHALA ATADZIWA  
KALE KUWERENGA?


YOSEFE, INE  
SINDIKUDZIWA, KOMA  
MULLINGU NDIYE  
AKUDZIWA. TINGODIKIRA,  
TIDZAONE KUTI  
ZIDZAKHALA BWANJI.




GENESIS 3:15; YESAYA 7:14, 9:7;  
MATEYU 1:18-23; LUKA 1:32-33

IWE NDI INE KHOLO  
LATHU NDI DAVIDE, NDIPO  
ANENERI ADANENA KUTI  
MESIYA ADZACHOKERA  
M'BANJA LA DAVIDE.

**NDIKUGANIZA CHINTHU CHINA. M'MUNDA UJA  
WA EDENI, MULLINGU ADALONJEZA KUTI MBEU YA MKAZI  
IDZAPHWANYA MUTU WA MBEU YA NJOKA. NDAZINDIKIRA  
TSOPANO! MWANA UYU SADZAKHALA MBEU YA  
MWAMLUNA, KOMA YA MKAZI. KANI! MULLINGU ADAKONZA  
ZIMENEZI KUCHOKERA PACHIYAMBI POMWE.**



YOSEFE NDI MARIYA ANKAKHALA KU NAZARETI WA KU GALILEYA, KOMA PADALI ULOSI WAKUTI MESIYA ADZABADWIRA KU BETELEHEMU WA YUDEA (MIKA 5:2). MARIYA TSOPANO ANKAYEMBEKEZA KUBALA MWANA WAKE MU MZINDA UMENE ANENERI SANAIKAMBEPO. SANKADZIWA ZA UNENERI UMENEWU, NDIPO PANALIBENSO CHIFUKWA CHOTI APITIRE KU BETELEHEMU, KUTALI NDITHU.



TAMVERANI, TAMVERANI, IZI  
ZACHOKERA KWA MFUMU YA KU ROMA,  
ZASINDIKIZIDWA NDI KAESARA MWINI WAKE,  
KUDZAKHALA KALEMBERA NDIPO ANTHU ONSE  
APITE KU MIZINDA IMENE ADABADWIRA  
KUTI AKALEMBETSE KALEMBERA  
WA MSONKHO.



YOSEFE, NDIYE  
KUTI UYENERA KUPITA  
KU BETELEHEMU.  
UDZAPITA MWANA  
AKABADWA.

SIZIKHALA BWINO  
NDIKAKUSIYA WEKHA,  
NDIYE KUTI ANTHU  
ADZAYAMBA KUDABWA.  
NDIPTA NDI IWE BASI.



MARIYA,  
NDIKANADZIWA  
SINDIKADAKUTENGA.  
MWINA  
TINGOBWERERA.

AI, NDIYENERA  
KUKHALA PAFUPI NAWA  
KUFIKIRA PAMENE MWANAYO  
ADZABADWA. PALIBE AMENE  
AKUMVETSA ZIMENE  
ZINATICHITIKIRAZI.

NGATI  
NKUTHEKA  
TIYENDE  
MWACHANGU.  
NDIYESA NTHAWI  
YAKWANA.

ZINAWATENGERA PAFUPIFUPI  
SABATA IMODZI KUYENDA MTUNDA  
WA MAMA LOSI NGATI 100.



NDIONA NGATI  
TINGAPEZE CHIPINDA  
CHOGONA M'NYUMBA  
INA YA ALENDO.






MARIYA,  
NDAPEZA ZAMBA  
WOTI  
ATITHANDIZE.

KODI MULIBE  
MALO  
M'NYUMBA YA  
ALENDOYO?

AI, NDI  
YODZAZA.



MUNAFUNITSITSA  
KUTI MWANA WANU  
ABADWIRE PABWINO.  
KOMA TAONANI  
WABADWIRA M'KHOLA  
LA NG'OMBE.

MUSADANDAULE.  
TSIKU LINA  
ADZALAMULIRA DZIKO  
LONSE LAPANSI  
AMENEYU.

AI NDITHU, KWA  
INE, MWANAYU  
AKUONEKA MONGA  
AONEKERA ANA  
ENA ONSE.

LUKA 2:1-7




NCHIYANI?  
*NDI*  
*MNGELO!*

ZIKWIZIKWI ZA  
ANGELO!

MUSAOPE, PAKUTI  
MULLINGU WANDITUMA  
KUTI NDIDZALENGEZE  
LTHENGA WABWINO KWA  
ANTHU ONSE, PAKUTI LERO  
WAKUBADWIRANI  
MPULUMUTSI MU MZINDA WA  
DAVIDE, AMENENEYO NDIYE  
MESIYA WA AYUDA,  
AMBUYE.



ULEMERERO KWA  
MULLINGU M'MWAMBAMWAMBA!  
MULLINGU WABWERETSA  
MTENDERE PA DZIKO LAPANSI  
POPEZA AMAFUNIRA ZABWINO  
ANTHU AKE.



CHIZINDIKIRO CHAKE NDI  
ICHI: MUKAPEZA KHANDA  
LITAKULUNGIDWA M'NSALU  
YOIKIRA MALIRO, LITAGONA  
MODYERA NG'OMBE.



**NZODABWITSA ZEDI!  
ANGELO KUONEKERA IFE!**

**IMANI KAYE  
MPAKA NDIUZE  
MKAZI WANGA!**

**KODI MWAMVA  
ZIMENE WANENA? MESIYA  
WABADWA MU ISRAELE.**

**MPULUMUTSI!  
MTENDERE KWA  
ANTHU! MWANA?  
TIYENI TIPITE  
TIKAMUONE!**

**NDIKUFUNA  
NDIPITE  
NDIKAONE.**



**MESIYA!**

PEPANI KUTI  
TIKUVUTITSANI,  
KOMA MNGELO  
ANATI TIBWERE  
KUNO.

ANGAMVETSE IZI  
NDANI, MULLINGU  
KUSANDUKA  
KHANDA?

LUKA 2:8-20

NTHAWI INAFIKA KUTI MARIYA  
NDI YOSEFE APEREKE MWANA  
WAKHANDAYO KWA WANSEMBE  
NDI KUPEREKA NSEMBE  
ZOLAMULIDZWAZO POTSATA  
MWAMBO WA AYUDA.



YOSEFE, AKA  
NKOYAMBA KUTI MWANAYU  
AFIKE KU KACHISI, NDIPO  
PALIBE AMENE AKUDZIWA  
KUNO KUTI YESU NDI  
KHRISTU.

NDIPO NDIYESA  
KUTI TISAUZE  
ALIYENSE. TIYENI  
TIDIKIRE  
MPAKA AKULE.






SIMEONI ANALI  
M'KACHISIMO.

NDI AMENEYO.  
TAMUDIKIRA  
NTHAWI YAITALI.


MARIYA, NDANI  
AMENEYO?

SINDIMDZIWA.  
PALIBE AMENE  
AMATIDZIWA  
KUNO.




WODALITSIKA NDINU YEHOVA,  
INU AMBUYE MULUNGU WATHU. TSOPANO  
NDIKHOZA KUFA MU MTENDERE, CHIFUKWA  
NDAONA CHIPULUMUTSO CHANU, MONGA  
MOMWE MUNALONJEZERA. ADZAKHALA  
KUWALA KWA ANTHU A MITUNDU INA NDI  
ULEMERERO KWA ISRAELE.

KOMA,  
MWAZINDIKIRA  
BWANJI?




MVERENI, MWANA  
UYU ADZACHITITSA  
KUTI AMBIRI MU  
ISRAELE ADZUKE NDI  
KUTI ENA AGWE, NDIPO  
ADZAMTSUTSA NDI  
KUDANA NAYE.

INDE, NDIPO MTIMA  
WANU LDZASWEKA  
POONA ZIMENE  
ZIDZAMCHITIKIRA.



TAONANI! MESIYA.  
WAFIKA KU KACHISI WAKE.  
LIYU NDIYE AMENE  
ANENERI ADANENA  
ZA IYE.

AMENEYO DZINA  
LAKE NDI ANA. MOYO  
WAKE WONSE WAKHALA  
AKUDIKIRA MESIYA.




**MNYAMATA IWE,  
MWANA UYU NDI KHRISTU,  
MPULLUMUTSI WA DZIKO  
LONSE LAPANSI.  
ADZAPULLUMUTSA AISRAELE  
KU MACHIMO AO.**

**KUCHOKERA NTHAWI IMENEYO,  
ANA ANKANENA ZA IYE KWA  
ONSE OFUNA CHIPULLUMUTSO.**

**LUKA 2:27-38**

M'MAIKO A KUMMAWA  
KUNALI ANTHU ENA AMENE  
ANKAPHUNZIRA ZINTHU  
ZAKALE NAFUNA KUDZIWA  
MULINGU. ANKADZIWA  
UNENERI WOKHUDZA MESIYA  
WODZABWERAYO. M'MALOTO  
NDI M'MASOMPHENYA,  
MULINGU ADAWAULULIRA  
KUTI WOLONJEZEDWA UJA  
WABADWA. KENAKA ADAONA  
NYENYEZI YODABWITSA  
ITALOZA KU DZIKO LA  
ISRAELE.






TACHOKERA KUTALI.  
DZIKO LIMENE TIKUPITALI  
NDI LACHILENDO. TAKHALA  
TIKUYENDA KWA MASABATA  
AMBIRIMBIRI.

NYENYEZI  
IKANAYENDABE.  
TIYILONDOLA  
NDITHU  
IMENEYI.




PA NTHAWI IMENEYO DZIKO LA ISRAELE LINALIBE MFUMU, POPEZA AROMA NDIWO AMENE ANKAWALAMULIRA. KOMA MFUMU YA AYUDA IMENE IDASANKHIDWA NDI AROMA, HERODE, INKALAMULIRA KU YERUSALEMU. ANTHU ANZERU AJA ANAPITA KWA HERODE KUTI AKAWAUZE ZA MFUMU IMENE INABADWAYO; KHANDA LIJA.





MFUMU HERODE,  
KWAFIKA ANTHU ATATU  
OLEMERA KWAMBIRI  
OCHOKERA KUMMAWA. AKUTI  
AKUFUNA MFUMU  
YATSOPANO YA ISRAELE;  
KHANDA.

KHANDA? MFUMU?  
MFUMU NDINE. BWERANI  
NAWONI KUNO NDIPO  
MUNDIBWERETSERENSO MKULU  
WA ANSEMBE NDI MLEMBI  
WA MALAMULO.



MWATI MWABWERA  
KUFUNA MFUMU  
YATSOPANO YA ISRAELE.  
MFUMU YAKHANDA?  
MUKUZIDZIWA BWANJI  
ZIMENEZI?

TINAONA NYENYEZI  
YAKE KUMMAWA  
NDIPO TABWERA  
KUDZAMUPEMBEDZA.

ALI KUTI?

SITIKUDZIWA  
BWINOBWINO.  
NCHIFUKWA  
CHAKE  
TABWERA  
KWA INU.

NDAITANITSA ANTHU  
OPHUNZIRA. TIONA NGATI  
AKUZIDZIWA ZIMENEZI.  
BWERANI M'CHIPINDA  
CHINO.


AKUTI ABWERA  
KUDZAPEMBEDZA MFUMU YA  
AYUDA, IYE AMENE ANENERI  
ADANENA ZA IYE KUTI ADZABWERA  
KUDZAPULUMUTSA ANTHU. KODI  
MABUKU ANU AMAKAMBAPO ZA  
MFUMU IMENEYI?

INDE, ANENERI  
AMBIRI ANANENA ZA  
KUBWERA KWAKE, KOMA  
SITIKHULLUPIRIRA KUTI  
UNENERI UMENEWU  
TINGANGOLYESA  
WACHIBWANA.

SINDILABADIRA  
CHILICHONSE PA ZA  
MAPHUNZIRO ANUWO.  
MWACHINDUNJI, KODI  
UNENERI UMENEWU  
UKUTANTHAUZANJI?

CHABWINO, MNENERI MIKA  
ADATI MESIYA ADZABADWIRA  
M'BETEHEMU KUCHOKERA  
M'FUKO LA YUDA.






TAMVERANI, INENSO  
NDIKUFUNA NDITAPEMBEDZA  
NAWO MFUMUYO. CHONCHO  
MUKAIPEZA MUNDIDZIWITSE  
KUMENE ILILI.


INDE MFUMU.  
TIKANGOMPEZA  
TIKUDZIWITSANI.

HERODE ANKACHITA MANTHA NDI  
MFUMU IMENE INABADWAYO,  
NDIPO ANAGANIZA ZOTI APHE  
MWANAYO AKADZIWA KOMWE ALILI.

A comic book illustration showing a scene with two men. On the left, a man with a beard and a crown with four crescent moons on his forehead looks towards the right. In the center, a man in a turban and a yellow and orange robe is speaking, with a large speech bubble coming from him. The background is dark with some blue and orange light effects.

ZINALI ZOCHITITSA  
CHIDWI NDITHU MMENE  
ALEMBI AJA ANADZIWIRA  
MALO ENIENI KUMENE  
MWANAYO ADZABADWIRA.  
KOMABE SANKAKHULLUPIRIRA  
ANENERI AOWO.

ZOLEMBA ZA ANENERI A  
KU ISRAELE NDI ZOPAMBANA  
ZEDI. SINDINAONEPO  
ZOLEMBEDWA ZACHINDUNJI  
CHONCHI.



**TAONANI!  
NYENYEZI  
YOMWE TIDAONA  
KUMMAWA  
KUJA!**

**KOMA IKUONEKA  
NGATI SINYENYEZI  
YOMWE TIDAIONAYO.  
SIKUYENDA NDI  
NYENYEZI ZINA,  
NDIPO NDI YOWALA  
KWAMBIRI.**


**MUONETSETSE  
PAMENE ILILIPO,  
NDIPO MAWA  
TIDZAITSA.**



**ONANI, YAIMA PAMWAMBA  
PA NYUMBA. KOMA KLINO SI KU  
BETELEHEMU. PAPITA MIYEZI  
YAMBIRI. MWINA MWAKE  
ADACHOKAKO.**

**TAYENDA  
ULENDO WAUTALI  
KWAMBIRI, NDIPO  
TAKHALA PANG'ONO  
KUFIKA KUMENEKO.**

**ZOONADI NDI  
NYENYEZI  
YODABWITSA. KOMA  
ILI PAFUPI ZEDI.**




SITIKUFUNA  
TIKUSOKONEZENI, KOMA  
TAYENDA ULENDU WA  
MASABATA AMBIRIMBIRI  
POFUNA KUDZAONA NDI  
KUPEMBEDZA MFUMU  
IMENE YANGOBADWAYI.

MUNADZIW  
A BWANJI?

TIMAWERENGA MALEMBO OYERA  
A ANTHU ONSE. ANENERI ANU ADALOSA  
ZA KUBWERA KWAKE, NDIPO NYENYEZI  
INAONEKA KUTI ITITSOGOLERE.  
NGAKHALE TSOPANO YAIMA  
PAMWAMBA PA NYUMBA YANUYI.






MODZICHEPETA  
TIKUPEREKA MPHATSO  
ZOCHEPAZI POLEMEKEZA  
MPULUMUTSI WA DZIKO LONSE  
LAPANSI. ADZATEMBENZIRA  
ANTHU AMBIRI KU  
CHILUNGAMO.


USIKU UMENEWO, MULLINGU ADAYANKHULA  
ANZERUWO M'MALOTO NDIPO ADAWALIZA  
KUTI ASADZIWITSE HERODE KUMENE KULI  
MWANAYO, KOMA KUTI ABWERERE KWAO  
PODZERA NJIRA INA. NDIPO MULLINGU  
ADAYANKHULANSO NDI YOSEFE, KUMLUZA  
KUTI ATHAWIRE KU IGUPTO, POPEZA  
HERODE AMAFUNAFUNA KUPHA MWANAYO.

MATEYU 2:9-12



ANTHU AKUMMAWA  
AJA ANDIPUSITSA. ADZERA  
NJIRA INA POPITA KWAO.  
NDIYE KUTI MWANA UJA  
ADAMPEZA NDIPO ANKACHITA  
MANTHA KUDZERA NJIRA  
YOMWEYI.

TUMIZANI ASILIKALI  
ANGA KU BETELEHEMU.  
MUWALIZE KUTI APHE MWANA  
ALYENSE WAMWAMUNA  
WOSACHEPERA  
ZAKA ZIWIRI.



ZAKA ZAMBIRI  
M'MBUYOMO, ANENERI  
ADALOSA ZA CHINTHU  
CHOMVETSA CHISONICHI  
KUTI CHIDZACHITKA  
M'BETEHEMU.

YOSEFE NDI MARIYA ADATHAWIRA  
NAYE YESU KU IGUPTO. MPHATSO  
ZA ANTHU ANZERU AJA  
ZIDAWATHANDIZA PA ULENDU WAO  
WOPITA KU IGUPTO KUMENE  
ANAKHALAKO KWA ZAKA ZIWIRI.



HERODE ATAMWALIRA, PAMENE  
YESU ANALI NDI ZAKA ZIWIRI,  
MULUNGU ADAWALAMULANSO  
KUTI ABWERERE KU ISRAELE.

ICHINSO CHIDAKWANIRITSA  
UNENERI WA M'BAIBULO: "MWANA  
WANGAYO NDIDAMUITANA KUTI  
ATULLUKE KU IGUPTO."





KODI ANTHUNU  
MUGWIRA  
NTCHITO TSIKU  
LONSE? BWERANI  
DZADYENI.

ATABWERAKO KU IGUPTO KUJA,  
MNGELO ADAUZA YOSEFE KUTI  
APITE AKAKHALE MU MZINDA  
WINA WALING'ONO WOTCHEDWA  
NAZARETE. ICHINSO  
CHIDAKWANIRITSA LINENERI  
WONENA KUTI IYE  
ADZATCHEDWA MNAZARETE.



**YEREMIYA 31:15; HOSEA  
11:1; MATEYU 2:13-23**

**YESU ANKAGWIRA  
NTCHITO YA UMISIRI WA  
MATABWA NDI BAMBO  
WAKE YOSEFE. ANAKULA  
MU MSINKHU NDI MU  
UZIMU, NDIPO ANALI  
WANZERU ZEDI.**

PAMENE YESU  
ANALI WA ZAKA 12,  
YOSEFE ANATENGA  
BANJA LAKE NDI  
KUPITA NALO  
KUPHWANDO KU  
YERUSALEMU.  
ADATENGA NKHOSA  
YAO YOTI  
AKAPEREKERE  
NSEMBE CHIFUKWA  
CHA MACHIMO AO.

ABABA, KODI  
NDINGATHE KUPITA  
NDI YESU KUKAONA  
KACHISI?

YESU, PITA NDI NKHOSAYI  
KWA ANSEMBE. AYENERA  
KUIWONA NGATI NDI YABWINO  
USANAFIKE MWAMBO WOIPEREKA  
MAWA LINO. TIPEZA PENNA  
POTI TIGONE USIKU UNO.





PATAPITA MASIKU  
AMBIRI, ATACHITA  
MWAMBO WA NSEMBE:


YOSEFE, YESU  
SINDIKUMPEZA,  
NDAYANG'ANA  
PALIPONSE. PALIBENSO  
AMENE WAMUONA  
TSIKU LONSELI.

NDIYESA TAMUSIYA  
KU *YERUSALEMU*.

KOMATU AMADZIWA  
KUTI TIKUNYAMUKA.  
NDIMAGANIZA KUTI ALI  
NDI ABALE ATHU ENA.


APATU TIYENERA  
KUBWERERANSO KU  
YERUSALEMU KUTI  
TIKAMUFUNEFUNE.





NONSENU MUMAVOMEREZA  
KUTI MESIYA ADZAKHALA MWANA  
WA DAVIDE, POPEZA ANENERI  
AMATERO. MUMAVOMERANSO KUTI  
DAVIDE ANAMUTCHULA KUTI  
AMBUYE, NGATI KUTI MESIYAYO  
NDI MULLINGU WAKE. NANGA  
TSONO MESIYA AKHALA BWANJI  
MWANA WA DAVIDE NDI AMBUYE  
AKE NTHAWI IMODZI,  
POKHAPOKHA...

LIYENERA KUSAMALA  
NDI MAGANIZO  
AMENEWO, PAMAPETO  
PAKE UKHOZA KUNYOZA  
MULLINGU.



KAPENATU MALEMBO  
OYERA AKULONDOLA  
KAPENANSO AI. KODI  
TIZIKHULUPIRIRA CHOKHACHO  
CHIMENE SICHITSUTSANA NDI  
ZIMENE TIDAZOLOWERA?

KOMA  
UKUGANIZA KUTI  
KUTANTHAUZIRA  
KWAKOKU NKOLONDOLA.  
AKULLIAKULU ATHUWA  
NDIWO ANGAZINDIKIRE  
ZINSINSI ZOZAMAZI.

YESAYA 9:7; LUKA 2:42-46; 2 TIMOTEO 3:16-17



LIYO ALI  
APOYO.

KODI CHOONADI  
CHIMAKHALA CHOZAMA?  
KODI MALEMBO OYERA  
SANAPEREKEDWE KUTI  
TIZIWAMVETSETSA?

KOMA ZONSE  
SIMUNGAZIONE MONGA  
ZILILIMU. TALIMUDI  
AMATI..."




YESU,  
TAYANG'ANA  
PONSEPONSE  
KUFUNA IWE.  
WATIZUNZIRANJI  
CHOTERE?

WAKHALA NDI IFE  
MASIKU AWIRI. MULI  
NDI MWANA  
WODABWITSA.



MUMANDIYANG'ANIRA  
NJI? KODI SIMUDZIWA  
KUTI NDIYENERA  
KUGWIRA NTCHITO YA  
ATATE ANGA?



SINDINAONEPO  
MNYAMATA  
WACHICHEPERE  
CHONCHI WODZIWA  
MALEMBO OYERA  
KWAMBIRI.

MAU OTI, 'FURABIDA' (ATATE)  
AMATANTHAUZA 'FAWU'  
(ATATE), NDI MAU AMENE  
YESU ANKAKONDA KUGWIRITSA  
NTCHITO POKAMBA ZA  
MULLINGU WA KUMWAMBA.

AMATANTHAUZA  
CHIYANI PONENA KUTI,  
"NDIYENERA KUMAGWIRA  
NTCHITO YA ATATE  
ANGA? KODI AMENE  
AMAMFUNAFUNA AJA  
SI ATATE AKE?"



YESU ANABWERERA NDI  
MAKOLO AKE NDIPO  
ANKAWAMVERA.  
ANAPITIRIZA KUGWIRA  
NTCHITO YA UMISIRI WA  
MATABWA NDIPO  
ANKAKULABE M'NZERU  
NDI MU MSINKHU.


POPEZA NTHAWI ZONSE  
ANKACHITA CHILINGAMO NDI  
KUFUNIRA ANZAKE ZABWINO,  
ANKAKONDEDWA NDI  
ALYENSE. ACHINYAMATA  
ANZAKE ANKAGWA MU  
LICHIMO, KOMA YESU  
ANKAMVERA MALAMULO ONSE  
A MULLINGU KUCHOKERA  
PANSI PA MTIMA WAKE.






MITENGO YANU NDI  
YABWINO KWAMBIRI, NDIPO  
MULIBE MMISIRI WONGA INU  
M'NAZARETE. NDI TENGANSO  
ZINA ZISANU NDI CHIMODZI  
ZOFANANA NDI  
CHIMENECHI.

KUMBUKIRANI KUTI ELIZABETI ATABALA MWANA PANAPITA MIYEZI 6  
KUTI MARIYA ABALE WAKE. MNGELO ADAUZA ZEKARIYA KUTI  
ADZAMUTCHE DZINA LAKE YOHANE, NDIPO KUTI ADZAKONZEKERETSA  
MITIMA YA ANTHU PA ZA KUBWERA KWA MESIYA. ZIMENEZINSO  
ZIDALOSEDWA NDI ANENERI AMBIRI ZAKA 500 ZISANACHITIKE IZI.



SIYANI NJIRA ZANU  
ZOIPA NDIPO MUZIMVERA  
MULLINGU, PAKUTI UFUMU  
WAKUMWAMBA WAKHALA  
PANG'ONO KUTI  
UKHAZIKITSIDWE. MUKAKONZA  
MITIMA YANU KUTI  
IDZALANDIRE MESIYA,  
NDIKUBATIZANI NDI  
MADZI.




KOMA PALI WINA AMENE  
AKUBWERA PAMBUIYO PANGA  
AMENE NDI WOPOSA INE,  
POPEZA ANALIPO INE KULIBE.  
SADZAKUBATIZANI M'MADZI, KOMA  
MU MZIMU WOYERA WA MULLUNGU  
MWINI WAKE. SIYANI MACHIMO  
ANU ZINTHU ZISANAKUIPIRENI.

TICHITE CHIYANI,  
YOHANE? MULLUNGU  
AFUNA TICHITENJI KUTI  
TIKHALE OLLUNGAMA?



NGATI MULI NDI  
MALAYA AWIRI NKUKUMANA  
NDI MUNTHU AMENE ALIBE,  
MPATSENI MALAYA AMODZI.  
NGATI MULI NDI CHAKUDYA  
NDIPO WINA ALI NDI  
NJALA, MDYETSENI.

CHITANI  
CHILINGAMO  
KWA ANTHU  
ONSE.




NANGA IFE OGWIRA  
NTCHITO M'BOMA,  
TICHITE CHIYANI KUTI  
TIKONDWERETSE  
MULLINGU? INE NDINE  
WOKHOMETSA  
MSONKHO NDIPO  
MNZANGAYU NDI WA  
KASITOMU.

MUSAMALANDIRE  
ZIPHUPHU. MUSAMAGWIRITSE  
NTCHITO UDINDO WANU  
NCHOLINGA CHOFUNA KULANDA  
ANTHU NDALAMA. KHALANI  
ACHILINGAMO NDI OYERA  
M'ZOCHITA ZANU ZONSE.

INE SINDINE WA MTUNDU  
WANU, SINDINENSO WA  
CHIPEMBEDZO CHANU. KOMA NANGA  
NDINGACHITE CHIYANI KUTI  
NDIKONDWERETSE MULUNGU?  
NDICHITE CHIYANI?



OSAMACHITIRA NKHANZA  
AMENE MUKUWALAMULIRA, NDIPO  
MUSAMABE KAPENA KUGWIRITSA  
NTCHITO UDINDO WANU NCHOLINGA  
CHOFUNA KULANDA ANTHU NDALAMA  
KAPENA KATUNDU. MUZIKHUTIRA  
NDI MALIPIRO ANU.




MAU AKUTI LIBATIZO  
AKUCHOKERA KU MAU  
ACHIGRIKI NDIPO  
AMATANTHAUZA, "KUNYIKA  
KAPENA KUMIZA."

IYE AMENE AKUDZA  
PAMBUYO PANGA NDI  
WAMPHAMVU KUPOSA INE,  
NDIPO SINDINGATHE  
KUMASULA NSAPATO ZAKE.  
ADZAKUBATIZANI NDI  
MZIMU WOYERA.

NGATI MUMUKANA NDI  
KUPITIRIZABE MACHIMO ANU,  
ADZAKULOWETSANI KU MOTO  
WA CHILANGO CHOSATHA.  
LEKANI KUCHIMWA LERO.

MALAKI 3:1; LUKA 3:2-18, 7:24, 27



INE  
SINDINE  
MESIYA.

IWE NDIWE YANI,  
AMENE UKULALIKA ZA  
MESIYA? UNGATIENZE  
CHIYANI ZA IWE?  
KODI IWE NDIWE

*AI, MONGA MOMWE  
ADANENERA MNENERI  
YESAYA, "INE NDINE MAU  
A WOFULLA M'CHIPULULU,  
KONZANI NJIRA  
YA MESIYA."*

MNENERI AMENE  
MOSE ADANENA KUTI  
ADZABWERA NDI  
KUDZATSOGOLERA  
ANTHU KUTI  
ABWERERENSO  
KWA MULLINGU?





NDANI ADAKUPATSA  
MPHAMVU ZA ULAMULIRO  
WOBATIZIRA ANTHUWA?


INE NDINE MTUMIKI CHABE,  
MKUPAMAME WA MESIYA, KOMA INU  
NDINU ANA A NJOKA. MUMAGANIZA KUTI  
POTI NDINU AYUDA, ANA A ABRAHAMU  
NDIYE KUTI NDINU ANA A  
MULUNGU.

MUYENERA KUSIYA MACHIMO ANU A  
KUNYADA NDI KUDZITUKUMULA. NKHWANGWA ILI  
KALE PA MUZU WA MTENGO, NDIPO MUDZADULIDWA  
NDI KUPONYEDWA M'MOTO WA CHIONONGEKO  
NGATI SIMUTEMBENUKA MTIMA.



YOHANE, UKUTI MESIYA  
AKUBWERA POSACHEDWAPA.  
UDZAMDZIWA BWANJI  
AKABWERA?

MNGELO WA MULLINGU  
ADANDILUZA KUTI AMENE NDIDZAMUONE  
MZIMU WA MULLINGU AKUTSIKIRA PA IYE  
NGATI NKHUNDA, AMENEYO NDIYE  
MESIYA WA ISRAELE, MPULUMUTSI  
WA DZIKO LONSE.



NDIDADZIWA KUTI NTHAWI  
YOTERE IDZAFIKA. MNGELO GABIRIELE  
ADANDIENZA KUTI NDIDZAMVA CHISONI  
CHACHIKULLU. NDIKADAKONDA BAMBO  
WAKO, YOSEFE, AKADAKHALA MOYO  
KUTI AONE ZIMENEZI.

UCHITA BWANJI?  
UYAMBA BWANJI?  
KODI UPITA KU  
KACHISI?

YOHANE ANAKHALA  
AKULALIKA KWA MIYEZI 6  
NDIPO YESU TSOPANO  
ANALI NDI ZAKA 30.

SINDIKUDZIWA. ATATE  
ANGA ADZANDIONETSA. POYAMBA  
NDIYENERA KUPITA KWA YOHANE  
KUTI AKANDIBATIZE. WATEMBENUZA  
ANTHU AMBIRI PA NYENGO  
YAKUBADWANSOYO.




KODI  
UDZABWERANSO  
KUDZANDIONA?

INDE, AMAI, SINDIDZAKUSIYANI,  
KOMA MUYENERA KULIMBA MTIMA.  
ZIDZACHITIKA ZINTHU ZINA PA INE  
ZIMENE SIMUDZAKONDWERA NAZO.

YESAYA 40:3; MATEYU 3:1-12; LUKA 3:15-18; YOHANE 1:19-27, 33

KONZEKERANI KUBWERA KWA MESIYA.  
INU ABAMBO TEMBENZANI MITIMA YANU KWA  
ANA ANU. MUYENERA KUKHALA ANZERU NDIPO  
NTHAWI NDI MPHAMVU ZANU MUZIGWIRITSE NTCHITO  
POPHUNZITSA ANA ANUWO MALAMULO A MULLINGU.  
ANA ANU OSAMVERA AKAONA KUKHULUPIRIKA KWANU,  
ADZATEMBENZA MITIMA YAO KWA INU NDIPO  
MABANJA ANU ADZACHIRITSIDWA.





NGATI IZI NDIZO  
MWATSIMIKIZA, NDIPO MUKUFUNA  
KUTSATA MESIYA AKABWERA, NDIYE  
BWERANI M'MADZI NDIPO  
NDIDZAKUBATIZANI NDI LIBATIZO WA  
KUTEMBENUKA MTIMA, NDIPO MESIYA  
AKABWERA ADZAKUKHULUKIRANI  
MACHIMO ANU.

YOHANE,  
NDIKUFUNA  
UNDIBATIZE.

NKOYENERA KUTI  
INU MUBATIZE INE.  
INU NDINU MUNTHU  
WOLUNGAMA.

YOHANE,  
NDIYENERA KUMVERA  
MALAMULO ONSE A  
MULLINGU. NDIDZACHITA  
MONGA MOMWE ATATE  
ANALAMULIRA  
ANTHU AKE.












MATEYU 3:13-17; LUKA 3:21-22





**LYU NDIYE  
MWANA WANGA  
WOKONDEDWA,  
NDIMAKONDWERA  
NAYE KWAMBIRI.**

**NDI AMENEYO,  
MWANAWANKHOSA  
WA MULLINGU  
AMENE AMACHOTSA  
MACHIMO A DZIKO  
LAPANSI!**




**WOYERA  
LIJA WA  
MULLINGU!**

**WAFIKA!**

**KHRISTU!**

**ADZAKHAZIKIT  
SA UFULMU!**

**LUKA 3:22; YOHANE 1:29-34; 1 YOHANE 2:1-2**



NTHAWI INA,  
KOMA PAKALI  
PANO AYENERA  
KUPAMBANA  
KAYE MAYESO!

AKUPITA KUTI?  
KODI SAOMBOLA  
DZIKOLI?


MAYESO  
ATI?

MAYESO AMENE  
ADAMU NDI ZIDZUKULU  
ZAKE ADALEPHERA.  
AYENERA KUKUMANA NDI  
MFUMU YA MDIMA.

ATATE ADAUZA YESU MWANA WAO KUTI  
ASALE ZAKUDYA KWA MASIKU 40.  
SADADYE CHAKUDYA CHILICHONSE. THUPI  
LAKE LITAFOOKA, SATANA ADAYESETSA  
KUMUZA IYE KUTI ASAMVERE ATATE  
AKE, NDI KUTI ADYE CHIFUKWA CHA  
NJALA IMENE ANKAMVAYO.

MUNTHU WOYAMBA, ADAMU,  
SANAMVERE MULLINGU NDIPO ADATAYA  
ZIMENE MULLINGU ADAMPATSA. YESU  
NDI MULLINGU WACHIKHALIRE, KOMA  
TSOPANO ANAKHALA MUNTHU NGATI  
IFE TOMWE. KODI AKANATHA  
KUPAMBANA MAYESERO AMENE ANTHU  
ONSE ADALEPHERA?





ATATHA MASIKU 40 AKUSALAWO, YESU ANAMVA NJALA  
NDIPO ANAFOOKA. TSOPANO ADADZIWA KUTI LUMPHAWI  
NDI CHIYANI, ADADZIWANSO ZA NJALA IMENE IMADYA  
THUPI LA MUNTHU. ADADZIWANSO TANTHAUZO LA  
KUKHALA WEKHA, KUSIYIDWA, KUDWALA, NDI KUFOOKA.

KWA MASIKU AMBIRI, SATANA ADAKHALA  
AKUSALITSA YESU NDI MAGANIZO OKAIKA NDI  
AMANTHA. PODZIWA KUTI YESU ANALI PAFUPI  
KUPAMBANA MAYESEROWO, NDI KUTI  
ANAFOOKA KWAMBIRI PA NTHAWI IMENEYI,  
SATANA ANACHITA CHINA CHAKE CHIMENE  
SAKONDA KUCHITA; ANAONEKERA YESU.





POPEZA NDINU  
MWANA WA  
MULINGU, MULI  
NDI LIFULU  
WAKUDYA  
CHAKUDYA.

MATEYU 4:1-3; LUKA 4:1-3; AROMA  
3:23, 5:12-21; AHEBRI 4:15


SATANA ADAYESA MUNTHU WOYAMBA,  
ADAMU, PAKUMUZA KUTI ADYE  
CHIPATSO CHOLETSEDWA. ANAYESETSA  
KUBWERETSA YESERO LOMWELO KWA  
MWANA WA MUNTHUYU AMENE ANKAMVA  
NJALA NDIPONSO ANAFOOKA KWAMBIRI.



LINALI YESERO LOOPSA KWA  
MUNTHU AMENE SANADYE  
CHILICHONSE KWA MASIKU 40.

A hand in a dark, textured sleeve holds a small, pale, human-like figure. The hand is positioned over a pile of dark, irregularly shaped objects that resemble bones or skulls. The background is a solid yellow color. A white, jagged-edged speech bubble is located in the upper right corner of the image.

ONANI, MUKHOZA  
KUSANDULIZA MWALA  
LIWU KUTI UKHALE  
MKATE NDI KUUDYA  
CHIFUKWA CHA NJALA  
YANUYI.



AI , AI SINDITERO, PAKUTI  
MALEMBO AMATI MUNTHU  
SADZAKHALA NDI MOYO NDI MKATE  
WOKHA, KOMA NDI MAU ALIWONSE  
AMENE MULLINGU AMAYANKHULA.

NDITSATE TSONO.  
NDIPITA NAWA KIMALO  
KOMWE LINGATHE  
KIMVERA MULLINGU.



MALEMBO AMATINSO,  
"USAMUYESE AMBUYE  
MULLINGU WAKO."


LITATI UDUMPHE KUCHOKERA  
PANO NDIPO ANGELO NKUBWERA  
KUDZAKUWAKHA, ANTHU ONSE ADZAONA  
ZIMENEZO NDIPO ADZAKULANDIRA IWE  
MONGA MESIYA, NDIPO NDIKUDZIWA KUTI  
CHIMENECHI NDI CHIMENE UNABWERERA.

UNAKAMBAPO ZA MALEMBO  
OYERA, NDIPO MALEMBOWO AMATI  
ANGELO ADZAKULANDIRA M'MANJA MWAO  
NDIPO ADZAKUTETEZA KUTI PHAZI LAKO  
LISASUMBE MWALA. TSOPANOTU IYI NDI  
NTHAWI YOTI UWAWONETSE  
MPHAMVU ZAKO.




NDIKUDZIWA KUTI LIMAKONDA  
DZIKO LAPANSI NDIPO UNABWERA  
KUDZALIPULLUMUTSA, TSONO  
NDIKLONETSA CHINA CHAKE,  
NDIKHULLUPIRIRA KUTI  
LDZACHIKONDA.

MATEYU 4:3-7


A comic book illustration showing two men on a cliff overlooking a city at sunset. The man on the left has long hair and a beard, wearing a white robe. The man on the right is wearing a hooded cloak and has his arms raised. The background shows a city skyline under a colorful sky. A large, jagged speech bubble is overlaid on the scene.

TAONA TSONO, KUCHOKERA PANO  
TIKHOZA KUONA MAIKO OTCHUKA A DZIKO  
LAPANSI. KODI SI A ULEMERERO  
WOPAMBANA? KUYAMBIRA NTHAWI IMENE  
ADAMU ANAGALLIKIRA ULAMULIRO WAKO,  
MAIKOWA NDIDAWATENGA KUKHALA ANGA.  
ANTHU AMANDIPATSA MAIKOWA NTHAWI  
ZONSE. DZIKO LONSE NDI LANGA. NDINE  
MULLINGU WA DZIKO LAPANSILI,  
OSATI IWE.

A comic book illustration showing two men on a cliff overlooking a city at sunset. The man on the left has a beard and long hair, wearing a white robe. The man on the right is wearing a dark, hooded robe and has his arms raised. The background features a city skyline and a body of water under a colorful sky.

KOMA NDIKHOZA KUKUPATSA  
LONSELI...UTATI WANDICHITIRA  
KANTHU KENA. UKANGOGWADA NDI  
KUNDIPEMBEDZA INE, NDIDZALEKERA  
POMWEPO KULAMULIRA DZIKOLI,  
NDIPO UKHOZA KULITENGA KUKHALA  
LAKO PAMODZI NDI ANTHU ONSE  
M'MENEMO. UKUTI BWANJI?





MALEMBO  
AMATI, "UZIPEMBEDZA  
YEHOVA MULLINGU  
NDIPO UZITUMIKIRA  
IYE YEKHAYO OSATI  
WINA AI." WALEPHERA;  
TSOPANO CHOKA.

SATANA ANACHOKA PAMASO PA KHRISTU. KWA NTHAWI  
YOYAMBA, SATANA ADAYESA MUNTHU AMENE  
ANALEPHERA KUMUNYENGA. YESU ANAPAMBANA  
MAYESO. TSOPANO DZIKO LAPANSI LINALI NDI MUNTHU  
MMODZI AMENE ANKAMVERA MULLINGU KOTHERATU.

MASIKU 40  
AMAYESERO ANATHA,  
KOMA YESU ANALI  
WOFOOKA KWAMBIRI.



ANGELO  
ANAMUBWERETSERA  
CHAKUDYA NDI MADZI  
NDIPO ANAMTUMIKIRA.  
ATAPEZA MPHAMVU,  
ANAPITA KUMENE  
YOHANE ANKALALIKA.



MATEYU 4:8-11; LUKA 4:14



<https://goodandevilbook.com/>